احترامِ مسلم

# Ulemu kwa Msilamu




SHAYKH-E-TARIQAT, AMEER-E-AHL-E-SUNNAT (MTSOGOLERI WA AHL-E-SUNNAT)
MUYAMBITSI WA DAWAT-E-ISLAMI, ALLAMAH MAULANA ABU BILAL
MUHAMMAD ILYAS
ATTAR QADIRI RAZAVI

اَلْحَمْدُ لِلّٰهِ رَبِّ الْعٰلَمِيْنَ وَ الصَّلٰوةُ وَ السَّلَامُ عَلٰى خَاتَمِ النَّبِيّٖن

اَمَّا بَعْدُ فَاَعُوْذُ بِاللّٰهِ مِنَ الشَّيْطٰنِ الرَّجِيْم بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْم

# Du'ā Powerenga Buku

Werengani Du'a (pempho) musanawerenge buku lachipembedzo kapena musanayambe phunziro lachisilamu; mudzakumbukira china chilichonse mwaphunzira, اِنْ شَآءَاللّٰه عَزَّوَجَلَّ:

اَللّٰهُمَّ افْتَحْ عَلَيْنَا حِكْمَتَكَ وَانْشُرْ
عَلَيْنَا رَحْمَتَكَ يَا ذَاالْجَلَالِ وَالْاِكْرَام

## Kumasulira

Yā Allah عَزَّوَجَلَّ! Titsegulireni makomo a maphunziro komanso a luntha ndipo tichitireni chisoni! E inu omwe muli wolemekezeka kwambiri komanso Awulemerero!

*(Al-Mustaṭraf, buku. 1, tsamba. 40)*

**Dziwani:** Mfunireni zabwino Mtumiki (Ṣalāt-'Alan-Nabī) ﷺ kamodzi musanayambe komanso kumapeto kwa Du'ā.

اِحترامِ مُسلِم

Ihtiram-e-Muslim

# Ulemu kwa Msilamu

Kabukuka kanalembedwa ndi Shaykh-e-Ṭarīqat Amīr-e-Aĥl-e-Sunnat, Muyambitsi wa Dawat-e-Islami 'Allāmaĥ Maulānā Abu Bilal Muhammad Ilyas Attar Qadiri Razavi دامت برکاتہم العالیہ mu chiyankhulo cha Urdu. **Nthambi Yomasulira** yamasulira kabukuka mu Chichewa. Ngati mungapeze cholakwika chilichonse pomasulira kapena pa kalembedwe, chonde dziwitsani nthambi yomasulira pa keyala kapena imelo ili m'mutsiyi ndi cholinga chopeza malipiro [Šawāb].

**Nthambi Yomasulira (Dawat-e-Islami)**

Aalami Madani Markaz, Faizan-e-Madinah, Mahallah Saudagran, Purani Sabzi Mandi, Bab-ul-Madinah, Karachi, Pakistan

**UAN:**☎+92-21-111-25-26-92 – Ext. 1262

**Email:**✉translation@dawateislami.net

**Ulemu kwa msilamu**

Kumasulira mchichewa kwa 'Ihtiram-e-Muslim'

◆

## MAWUFULU ONSE ASUNGIDWA

UMWINI © 2025 Maktaba-tul-Madinah

---

Palibe gawo la bukhuli lomwe lingathe kusindikizidwanso, kapena kufalitsidwa, mwa njira iliyonse, kapena yamagetsi, yamakina, yojambulira, kujambulitsa kapena mwanjira ina iliyonse, popanda chilolezo cholembedwa choyambirira cha Maktaba-tul-Madinah.

---

| | |
|---|---|
| **Kufalitsa:** | Rabi'-ul-Awwal, 1447 AH – (Oct, 2025) |
| **Wofalitsa:** | Maktaba-tul-Madinah |
| **Kuchuluka:** | - |
| **ISBN:** | - |

## KUTHANDIZA

Khalani omasuka kulumikizana nafe ngati mukufuna kuthandizira kusindikidza kwa buku lachipembedzo kuti likhale Isal-e-Sawab kwa achibale anu omwe anamwalira.

**Maktaba-tul-Madinah**

Aalami Madani Markaz, Faizan-e-Madinah MahallahSaudagran,
Purani Sabzi Mandi, Bab-ul-Madinah, Karachi, Pakistan

✍ **Email:** maktabaglobal@dawateislami.net – maktaba@dawateislami.net

✆ **Phone:** +92-21-34921389-93 – 34126999

💻 **Web:** www.dawateislami.net

# ZANKATIMU

Ulemu Kwa Msilamu....................1
Ubwino Wonfunira zabwino Mtumiki (Salat-'Alan-Nabi) ﷺ....1
Ndalama yabodza....................1
Dawat-e-Islami ikufuna chani?....................2
Anthu atatu adzalandidwa Kumwamba poyamba....................3
Tanthawuzo la Dayyoos....................3
Nkazi wovala zovala za amuna amalandidwa Kumwamba....................5
Kulemekeza m'bale wankulu....................6
Phunzitsani ana anu makhalidwe....................6
Chifukwa cholephelera kukhala ndi chikhalidwe cha Madani pakhomo....................7
Kodi tingapulumutse bwanji achibale athu ku Gehena?....................8
Kulemekeza achibale....................9
**NGALE ZA MADANI ZA KULUMIKIZANA BWINO NDI ACHIBALE**....................9
Tanthawuzo la Silah Rihmi [kuchitira bwino achibale]....................9
Ndizokakamiza kuchitira achibale ena mwachifundo....................10
Kodi 'Zu-Rihm Mahram' komanso 'Zu-Rihm' zimatanthawuza chani?....................11
Kodi munthu ayenera kuchita chani ngati achibale ali m'mayiko ena?....................13
Njira yodulira ubale....................13



www.dawateislami.net

Khalani ndi pawubale ndi amene akudula ubale ndi inu ..............14
Yanjanani ndi abale omwe sakondwera nanu ...............................14
Ubwino wa kusisita mutu wa mwana wamasiye ............................15
Yesetsani kusunga ubale ndi nkazi ...............................................16
Ubwino wa kufatsa pa nkazi...........................................................17
Khululukirani nkazi........................................................................17
Mchere wambiri mu chakudya .......................................................17
Ufulu wa mamuna ..........................................................................19
Musachoke pakhomo lamamuna ...................................................19
Chifukwa chimene akazi ambiri akakhalire ku Gehena ................20
Ufulu wa anthu oyandikana nawo.................................................20
Chiphaso cha makhalidwe abwino................................................21
Kodi Mtsogoleri wa Qafilah akuyenera kukhala ndi makhalidwe otani? ..................................................................................................22
Chilichonse chokhala chowonjezera chiyenera kuperekedwa kwa ena ..................................................................................................23
Mudzafunsidwa za amene ali pansi panu.......................................23
Kugawa Ntchito ..............................................................................24
Perekani mpando wanu kwa ena ...................................................25
Ulendo ndi Madani Qafilah.............................................................26
Usatenge malo ochuluka.................................................................27
Ndikutsatira Sunnah kupereka malo kwa amene akubwera kumene...........................................................................................27
Kutsitsa mawu ................................................................................29



www.dawateislami.net

Kudumpha m'makosi....................29
Kulowelera anthu awiri popanda chilolezo....................30
Kusunga malo poyika nsalu....................31
Musapweteke ntima wa munthu aliyense....................32
Uswa-e-Hasanah....................33
Ena mwa makhalidwe abwino a Mtumiki Woyera ﷺ ....................33
Kudula ubale ndiko Haram: Ngale 13 za Madani ....................40
Mawu Asanu ndi Awiri a Mtumiki Woyera ﷺ....................40



www.dawateislami.net

اَلْحَمْدُ لِلّٰهِ رَبِّ الْعٰلَمِيْنَ وَالصَّلٰوةُ وَالسَّلَامُ عَلٰى خَاتَمِ النَّبِيّٖنَ
اَمَّا بَعْدُ فَاَعُوْذُ بِاللّٰهِ مِنَ الشَّيْطٰنِ الرَّجِيْمِ بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْمِ

# Ulemu Kwa Msilamu

## Ubwino Wonfunira zabwino Mtumiki (Salat-'Alan-Nabi) ﷺ

Mneneri wa Chifundo صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati, 'Woyandikira kwambiri kwa ine pa Tsiku la Chiweruzo adzakhala yemwe akundifunira ine zabwino (Salat).'

*(Sunan-ut-Tirmizi, vol. 2, pp. 27, Hadees 484)*

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Ndalama yabodza

Wopembedza moto ankasokesa zovala zake kwa Sayyiduna Shaykh Abu 'Abdullah Khayyaat رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه ndipo ankapereka ndalama yabodza nthawi zonse, ndipo iye رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه ankavomereza akudziwa. Nthawi ina, iye panalibe, wophunzira wake sanavomereze ndalama yabodza kuchokera kwa wopembedza motoyo. Pamene Sayyiduna Shaykh Abu 'Abdullah Khayyaat رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anabwerera ndikudziwa za vutoli, iye رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anafunsa wophunzira wake, 'Chifukwa chani sunatenge ndalamayo? Kwa zaka zambiri, iye wakhala

akundipatsa ndalama yabodza ndipo ine ndakhala ndikulandira nthawi zonse kuti asadzayipereke kwa Msilamu wina .'

*(Ihya-ul-'Uloom, vol. 3, pp. 87)*

## Dawat-e-Islami ikufuna chani?

Wokondedwa abale achisilamu! Kodi mwawona! Makolo athu achipembedzo رَحِمَهُمُ اللّٰهُ anali ndi chikondi chenicheni kwa Asilamu ena. Ankapirira kusapeza kwawo kuti angopulumutsa Asilamu ena achilendo ngakhale ku vuto losayembekezereka, pamene masiku ano, m'bale akuwoneka akubera m'bale wake. Gululi la Dawat-e-Islami la padziko lonse lapansi likufuna kubwezeretsa zikumbukiro za makolo athu achipembedzo رَحِمَهُمُ اللّٰهُ. Dawat-e-Islami imachotsa chidani ndi kufalitsa chikondi. Msilamu aliyense ayenera kuyenda nthawi zonse ndi ma Madani Qafilah motsagana ndi okonda Mtumiki kuti aphunzire ma Sunnah, kulemba nkabuku konse ka Madani In'amaat pochita Fikr-e-Madinah ndikukapereka kwa m'bale woyenera kumayambiriro kwa mwezi uliwonse wachisilamu. Chifukwa cha Mtumiki wokondedwa Mustafa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم, chidwi cholemekeza Asilamu chidzakula, اِنْ شَآءَاللّٰه. Ngati tonse tilemekezana kuchokera pansi pa ntima, gulu lathu lidzasandukanso Munda wokongola, wokopa, wonunkhira bwino komanso wobiriwira wa Madinah wokhala ndi maluwa osiyanasiyana, اِنْ شَآءَاللّٰه.

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Anthu atatu adzalandidwa Kumwamba poyamba

Makolo ndi ﴿ذَوِی الْاَرْحَام﴾ [Zawil-Arhaam] (ndiye kuti, omwe ali ndi ubale wamagazi woyandikana) ayenera kulemekezedwa kwambiri komanso kuchitiridwa ubwino m'dera, koma mwatsoka, chidwi chochepa kwambiri chikuperekedwa pa nkhaniyi tsopano. Anthu ena amawoneka odzichepetsa komanso ochezeka pagulu koma amachitira nkhanza achibale awo, makamaka makolo awo. Nayi Hadeeth kwa anthu otere. Sayyiduna ‘Abdullah Ibn ‘Umar رَضِیَ اللّٰہُ عَنۡہُمَا ananena kuti Mtumiki Wankulu komanso Woyera صَلَّی اللّٰہُ عَلَیۡہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم anati, ‘Anthu atatu sadzalowa Kumwamba: iye amene amavutitsa makolo ake; Dayyoos komanso nkazi amene amatengera mavalidwe (mawonekedwe) a chimuna.’ *(Majma’-uz-Zawaid, vol. 8, pp. 270, Hadees 13431)*

## Tanthawuzo la Dayyoos

Hadees yapitayi ikunena kuti Dayyoos komanso amene amavutitsa makolo ake sadzalowa Kumwamba. Dayyoos ndi munthu yemwe samasamala za khalidwe (losayenera) la nkazi wake kapena nkazi wina wa Mahram, ndi amuna ena. *(Durr-e-Mukhtar, vol. 6, pp. 113)* Ndiye kuti, omwe ali ndi mphanvu yoletsa amayi awo, akazi awo, alongo awo ndi ana aakazi achichepere ndi ena wotero. koma osawaletsa kuyendayenda opanda chophimba m'misewu, misika, malo ogulitsira, ndi malo osangalalira osiyanasiyana; komanso omwe

sawaletsa kulankhula momasuka ndi anansi osakhala Mahram, achibale, antchito, alonda ndi madalayivala ndi ma Dayyoos ndipo alandidwa Kumwamba, oyenera ku Ng'anjo Kumbukirani! Kupatula anthu ena osakhala Mahram, Shari'ah inanena kuti ndikofunikira kuvala chophimba kwa azibale onse oyamba achimuna komanso achikadzi, nkazi wa m'bale wa abambo ake ndi amayi ake, mwamuna wa mlongo wa amayi ake ndi wa mlongo wa abambo ake, mlamu wankazi ndi mlamu wamwamuna. Ngati nkazi sakutsatira chophimba cha Shar'i kwa iwo, adzayenera ku Ng'anjo ya Moto. Ngati mwamuna wake samuteteza ku tchimo ili mpaka pamene angathere, ndiye kuti iye ndi Dayyoos malinga ndi Shari'ah ndipo poyamba sadzapatsidwa Kumwamba, akuyenera ku Ng'anjo ya moto. Dayyoos yemwe amachita ntchimo ili poyera ndi Faasiq-e-Mu'lin, osayenera kutsogolera Salah komanso kuperekera umboni. Wokondedwa abale achisilamu! Chitani chizolowezi choyenda ndi ma Madani Qafilah, kulemba nkabuku konse ka Madani In'amaat tsiku lililonse ndikulipereka kwa m'bale woyenera kudera lanu mwezi uliwonse. إِنْ شَآءَاللّٰه, matenda a machimo kuphatikiza matenda oyipa a u Dayyoos adzachira chifukwa cha Mtumiki wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم. Kunena kwa Mtumiki Woyera صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم yemwe amayang'ana pansi mwamanyazi, A'la Hadrat رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anapempha pamaso pa Mulungu:

*Ya Ilahi! Rang la-ayn jab mayri bay baakiyan*

*Un ki neechi neechi nazron ki haya ka sath ho*



www.dawateislami.net

*(Hadaiq-e-Bakhshish)*

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Nkazi wovala zovala za amuna amalandidwa Kumwamba

Zanenedwa mu Hadees kuti Nkazi amene amatengera kachitidwe ka chimuna adzalandidwa Kumwamba. Nkazi amene amavala zovala za amuna, nsapato, kapena amakhala ndi kametedwe ka tsitsi kachimuna amayeneranso chilango chomwecho. Masiku ano, anthu samasamala za nkhaniyi powaveka ana. (Allah عَزَّوَجَلَّ aletse) nthawi zina, anyamata amavekedwa zovala za atsikana kuwapangitsa iwo kuwoneka ngati atsikana. Momwemonso, atsikana samangovekedwa malaya ndi mabuluku okhala ndi zipewa za amuna ndizina zotero., komanso amametedwa kametedwe ka tsitsi ka ntundu wachinyamata, zomwe zimawapangitsa kuwoneka ngati anyamata.

Sadr-ush-Shari'ah, Badr-ut-Tareeqah, 'Allamah Maulana Mufti Muhammad Amjad 'Ali A'zami رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anati, 'Kupaka Henna m'manja ndi mapazi anyamata mosafunikira sikololedwa. Nkazi akhoza kupaka Henna m'manja ndi mapazi ake koma adzakhala wochimwa, ngati apaka Henna m'manja kapena mapazi anyamata. *(Bahar-e-Shari'at, vol. 3, pp. 428)*

Musawaveke ana anu zovala zomwe zili ndi zithunzi za zinthu zamoyo. Musapake zophoda nzikhadabo pa zala za ana. Azimayi sayenera kugwiritsanso ntchito zophoda nzikhadabo pa zala zawo chifukwa madzi samafika nzikhadabo zomwe zaphodedwa ndipo motero Wudu ndi Ghusl zimakhala zosavomerezeka.

## Kulemekeza m’bale wankulu

Pamodzi ndi makolo, achibale ena monga abale ndi alongo ayeneranso kulemekezedwa. Pambuyo pa abambo, agogo ndi m’chimwene wankulu ndi oyandikira kwambiri pakuti m'chimwene wankulu ndi mlowam’malo wa abambo. Mneneri Woyera صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati, ‘Ufulu wa n'chim wankulu pa n'chimwene wake wan’ng'ono uli ngati ufulu umene abambo ali nawo pa ana awo.’

*(Shu’ab-ul-Iman, vol. 6, pp. 210, Hadees 7929)*

## Phunzitsani ana anu makhalidwe

Makolo ayeneranso kupereka chidwi chokwanira pakukwaniritsidwa kwa ufulu wa ana awo. M'malo mowapangitsa kukhala 'amakono', ayenera kuyesetsa kuti ana awo atsatire Sunnah, kuwaphunzitsa makhalidwe abwino, kuwapatula kwa anzawo akhalidwe loyipa ndikuwapangitsa kuti alowe mu chikhalidwe cha Madani chomwe chimalimbikitsa Sunnah. Ayenera kuwalepheretsa kuchita zizolowezi zoyipa

monga kuwonera mafilimu ndi madrama, kutenga nawo mbali m'miyambo ndi nzikhalidwe zoyipa kumene nyimbo zimayimbidwa, kuwapangitsa anthu kusalabadira kukumbukira Allah عَزَّوَجَلَّ.

Masiku ano, makolo mwina amachiwona ngati ufulu wofunika kwambiri wa ana awo kuwapatsa maphunziro oyenera komanso luso lililonse ndi ukatswiri womwe angathe kupeza mmoyo. Kalanga ine! Thupi ndi zovala za mwanayo zimapulumutsidwa ku litsiro koma palibe kuyesetsa kumatengedwa kuti ntima ndi ntchito zake ziyeretsedwe. Mtumiki wokondedwa komanso wodala صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati, 'Ndibwino kuti munthu aphunzitse ana ake makhalidwe kusiyana ndi kupereka Saa' imodzi (ndiye kuti, pafupifupi 4 kilogramu ya tirigu) mu sadaka.' *(Sunan-ut-Tirmizi, vol. 3, pp. 382, Hadees 1958)*

Iye صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ananenanso, 'Palibe abambo amene anapereka kalikonse kwa mwana wake wabwino kuposa makhalidwe abwino.' *(Ibid, vol. 3, pp. 383, Hadees 1959)*

## Chifukwa cholephelera kukhala ndi chikhalidwe cha Madani pakhomo

Mwatsoka, kulibe chikhalidwe cha Madani m'nyumba zathu zambiri masiku ano ndipo ife tokha ndife amene tikuyambitsa vutoli. Nthabwala zathu, kunyoza, kusachita ulemu, makhalidwe oyipa, ndi kusasamala kwambiri ndizo zifukwa za

vutoli. Abale athu achisilamu ena amakhala mwawulemu komanso modzichepetsa ndi ena koma 'amabangula' ngati nkango wawukali kunyumba. Izi zimayambitsa kuwonongeka kwa ulemu wa munthu pakhomo.

Kumbukirani! Kusakhala bwino kwanu ndiko chopinga chachikulu pakukonza banja lanu. Chenjerani! Ngati simukonza makhalidwe anu ndipo osayesetsa modzichepetsa komanso mwawulemu kuti musinthe banja lanu, mutha kuthera mu chilango cha Ng'anjo ya Moto. Allah عَزَّوَجَلَّ Walankhula mu Qur'an Yoyera, gawo 28, Surah At-Tahrim, vesi 6:

يٰۤاَيُّهَا الَّذِيْنَ اٰمَنُوْا قُوْۤا اَنْفُسَكُمْ وَ اَهْلِيْكُمْ نَارًا وَّ قُوْدُهَا النَّاسُ وَ الْحِجَارَةُ

*E inu amene mwakhulupirira, dzipulumutseni inu ndi banja lanu ku moto umene mafuta ake ndi anthu komanso miyala.*

*[Kanz-ul-Iman (Kumasulira kwa Qur'an)] (Gawo 28, Surah At-Tahrim, vesi 6)*

## Kodi tingapulumutse bwanji achibale athu ku Gehena?

Ponena za vesi lomwe layikidwa m'mwambali, zanenedwa mu Khaza`in-ul-'Irfan: (Dzitetezeni nokha ndi achibale anu ku moto wa Gehena) pakunvera Allah عَزَّوَجَلَّ komanso Mtumiki Wake Wokondedwa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم, kuchita mapemphero, kuleka

machimo, kutsogolera achibale anu ku zabwino ndi kuwaletsa zoyipa komanso kuwaphunzitsa chidziwitso ndi makhalidwe.'

## Kulemekeza achibale

Achibale onse ayenera Kusamalidwa mwawubwino. Sayyiduna 'Aasim رَضِیَ اللّٰہُ عَنۡہُ ananena kuti Mtumiki wa Chifundo صَلَّی اللّٰہُ عَلَیۡہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم anati, 'Aliyense amene akufuna moyo wawutali, kuwonjezereka kwa chakudya chake ndi chitetezo ku infa yoyipa, ayenera kupitiriza kuwopa Allah عَزَّوَجَلَّ ndikukhala ndi achibale ake mwachifundo.'

*(Al-Mustadrak, vol. 5, pp. 222, Hadees 7362)*

Mtumiki wokondedwa komanso wodala صَلَّی اللّٰہُ عَلَیۡہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم anati, 'Amene akudula mawubale sadzalowa Kumwamba.'

*(Sahih Bukhari, vol. 4, pp. 97, Hadees 5984)*

# NGALE ZA MADANI ZA KULUMIKIZANA BWINO NDI ACHIBALE

## Tanthawuzo la Silah Rihmi [kuchitira bwino achibale]

Zanenedwa patsamba 201 mpaka 203 la gawo la khumi ndi chisanu ndi chimodzi la Bahar-e-Shari'at – buku la masamba 312 lolembedwa ndi Maktaba-tul-Madinah – Nthambi yosindikiza ya Dawat-e-Islami: ﴾صِلَۃ رِحۡم﴿ [Silah-Rihm]

imatanthawuza kukhazikitsa ubale, ndiye kuti kuchitira achibale zabwino zilizonse ndikuwachitira mwachifundo. Ummah wonse umagwirizana kuti Silah-Rihm [ndiye kuti kuchitira zabwino achibale] ndi Wajib ndipo kudula ubale ndi Haraam.

## Ndizokakamiza kuchitira achibale ena mwachifundo

Kodi ndi achibale ati amene ayenera kuchitiridwa mwachifundo monga ndi wa Wajib? Akatswiri ena anati ndi 'Zu-Rihm Mahram' ndipo ena anati ndi achibale a Zu-Rihm ngakhale kuti ndi Mahram kapena ayi. Zikuwoneka kuti lamulo lachiwiri ndilolondola kwambiri. Mahadeeth ali ndi lamulo losaweruzika lochitira achibale mwachifundo. Qur'an Yoyera inanenanso motsindika ﴿ذَوِی الْقُرْبٰی﴾ (oyandikananawo). Komabe, popeza pali milingo yosiyanasiyana ya mawubale, palinso milingo yosiyanasiyana yochitira achibale mwachifundo. Makolo ali ndi udindo wawukulu kwambiri. Pambuyo pa iwo pali udindo wa 'Zu-Rihm Mahram' (ndiye kuti achibale omwe kuchitanawo ukwati ndi Haraam mpaka kalekale chifukwa cha ubale wa Nasabi [ndiye kuti wochokera ku m'badwo]). Pambuyo pa iwo pali udindo wa achibale otsala, kutengera ubale wapafupi womwe ali nawo. *(Rad-dul-Muhtar, vol. 9, pp. 678)*

◆ ◆ ◆

## Kodi 'Zu-Rihm Mahram' komanso 'Zu-Rihm' zimatanthawuza chani?

Allah عَزَّوَجَلَّ analankhula mu vesi 83 la Surah Al-Baqarah:

وَ بِالْوَالِدَيْنِ اِحْسَانًا وَّ ذِی الْقُرْبٰی

*Ndipo khalani okoma ntima kwa makolo ndi achibale.*

Pofotokoza vesi ili, wofotokoza wotchuka, Hakeem-ul-Ummat, Mufti Ahmad Yar Khan رَحۡمَةُاللّٰہِعَلَیۡه anati mu Tafseer-e-Na'eemi: Ndipo mawu akuti ﴿قُرْبٰی﴾ amatanthawuza achibale, ndiye kuti achitireni achibale anu mwachifundo. Popeza ubale wa munthu ndi achibale ake umapangidwa kudzera mu ubale wa makolo ake ndipo kukoma ntima kwa achibale ake kwa iye kumakhala kochepa kuposa kwa makolo ake, ufulu wa achibale umakhalanso wofewa kuposa wa makolo. Nawa malangizo ena pankhaniyi:

Malangizo oyamba: ﴿ذِی الْقُرْبٰی﴾ [Zil-Qurba] ndi achibale omwe ubale wawo umapangidwa kudzera mu ubale wa makolo ndipo umatchedwanso ﴿ذِی رِحۡم﴾ [Zi-Rihm]. Pali magulu atatu a iwo: Loyamba, achibale abambo monga agogo amuna ndi akazi, m'bale ndi mlongo wa abambo ndi ene otero. Lachiwiri, achibale a amayi monga agogo a amayi ndi akazi, m'bale ndi mlongo wa amayi ndi abale a Akhyaafi (ndi alongo, ndiye kuti abale apantima ndi alongo apantima omwe amayi awo ndi omwe amodzi koma abambo awo ndi osiyana). Chachitatu,

achibale a makolo onse monga m'bale ndi mlongo weniweni. Aliyense amene ali ndi ubale wapafupi ali ndi ufulu wawukulu.

Malangizo achiwiri: Pali magulu awiri achibale: Pansi pa gulu limodzi pali omwe kuchitanawo Nikah ndi Haraam, ndipo amatchedwanso Zi-Rihm Mahram monga m'bale ndi mlongo wa bambo ndi mayi (Zi-Rihm Mahram ndi achibale apafupi kotero kuti ngati mmodzi wa iwo akuyenera kukhala mwamuna ndipo wina nkazi, ndiye kuti Nikah ndi Haraam mpaka kalekale pakati pawo. Izi zikuphatikizapo, mwachitsanzo, bambo, mayi, mwana wamwamuna, mwana wankazi, m'bale, mlongo, m'bale ndi mlongo wa bambo ndi omwe amayi, mwana wamwamuna komanso mwana wankazi wamwamuna ndi ena otero.) Ndikofunikira kuwathandiza panthawi yawo yosowa, ndipo amene sachita izi ndi wochimwa. Pansi pa gulu lina pali achibale omwe kuchita nawo Nikah ndi Halal; monga ana a abambo ndi amayi abambo ndi a azakhali a amayi. Ndi Sunnah Muakkadah [ndiye kuti Sunnah yotsindikidzidwa kwambiri] ndipo ndi ntchito yopeza mphotho yambiri kuwachitira bwino komanso ndi makhalidwe abwino. Kumbukiraninso kuti kuchitira achibale onse komanso Asilamu onse ndi makhalidwe abwino ndikofunikira ndipo kupanga zowapweteka mmaganizo ndi Haraam. *(Tafseer 'Azeezi)*

Malangizo achitatu: Achibale akutali saphatikizidwa mu Zi-Rihm. Komabe, ena mwa iwo ndi Mahram monga apongozi



www.dawateislami.net

aakazi ndi amayi a Rada`ee [ndiye kuti nkazi amene sanabereke mwana koma wamuyamwitsa nkati mwa zaka ziwiri ndi theka malinga ndi kalendala ya Hijri]. Ena mwa iwo si Mahram koma ali ndi ufulu. Ngakhale anansi ali ndi ufulu koma ufulu umenewu suphatikizidwa mu vesi ili chifukwa limatanthawuza Zi-Rihm ndi achibale ena. *(Tafseer-e-Na'eemi, vol. 1, pp. 447)*

## Kodi munthu ayenera kuchita chani ngati achibale ali m'mayiko ena?

Ngati munthu ali m'dziko lachilendo, ayenera kukhala akulemberana makalata ndi achibale ake kuti ubale usaduke. Ngati n'kotheka, ayenera kubwera kudziko lake kuti ubale kwa achibale ake ulimbitsike. Izi zidzakulitsanso n'gwirizano pakati pa achibale. *(Rad-dul-Muhtar, vol. 9, pp. 678)*

Mosiyana ndi kale pamene ngakhale kutumiza makalata kunkatenga nthawi yayitali, ndikosavuta m'nthawi zamakono kulumikizana. Ngati n'kotheka, munthu akhoza kulumikizana ndi achibale ake kudzera pa imelo kapena lamya. Izi ndi njira zowonjezera chikondi.

## Njira yodulira ubale

Pamene wachibale aliyense apempha thandizo lokwaniritsa chosowa chake, tiyenera kumuthandiza chifukwa kukana pempholi kuli ngati kudula naye ubale. *(Durad, pp. 323)*



www.dawateislami.net

Kumbukirani kuti kudula ubale (ndiye kuti, kudulitsa ubale) ndi Haram.

## Khalani ndi pawubale ndi amene akudula ubale ndi inu

Kuchitira ubwino sikungotanthawuza kuchitira ubwino achibale omwe anakuchitirani chabwino. Izi ndizo kuti kusinthanitsana. Mwachitsanzo, kutumiza mphatso kwa wachibale amene wakutumizirani mphatso kapena kupita kunyumba kwa amene akubwera kwanu. Kwenikweni, kuchitira ubwino kumatanthawuza kukhazikitsa ubale ndi amene akudula ubale ndi inu ndikusasamala za wachibale amene akukunyalanyazani ndikukhala kutali ndi inu.

*(Rad-dul-Muhtar, vol. 9, pp. 678)*

## Yanjanani ndi abale omwe sakondwera nanu

Abale achisilamu okondedwa! Ngati pali mikangano pakati pa inu ndi achibale anu, inu muyenera kukhala oyamba kulumikizana nawo. Ndikukupemphani mwachikondi cha Madani kuti muyanjane nawo kuchokera pansi pa ntima ngakhale atakhala olakwa. Komabe, ngati pali chifukwa cha Shar'i chokulepheretsani kuyanjana nawo, ndiye kuti muyenera kusiya kutero. Chifukwa cha Mtumiki wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم komanso chifukwa cha kuyenda ndi ma Madani Qafilah mwezi uliwonse, kulemba nkabuku konse ka Madani In'amaat ndikukalipereka kwa m'bale woyenera kumayambiriro kwa



www.dawateislami.net

mwezi uliwonse wachisilamu, اِنْ شَآءَاللّٰه, mudzapeza chikondi chachikulu cholemekeza Asilamu kotero kuti mikangano yanu yonse ndi achibale anu idzathetsedwa ndipo nawonso adzalowa mu chikhalidwe cha Madani cha Dawat-e-Islami, اِنْ شَآءَاللّٰه.

*Sab shakar ranjiyan* *Door haun gi miyan*

*Qafilay mayn chalayn* *Qafilay mayn chalo*

***Kumasulira:*** *Kusiyana konse kudzachotsedwa. Yendani ndi Madani Qafilah.*

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Ubwino wa kusisita mutu wa mwana wamasiye

Mnyamata kapena mtsikana wosakhwima yemwe abambo ake anamwalira amadziwika kuti mwana wamasiye. Mnyamata kapena mtsikanayo akakula, malamulo a mwana wamasiye sangagwiritsidwenso ntchito pa iwo. Pali mphotho yayikulu yochitira mwachifundo ana amasiye. Mtumiki wa Chifundo, Nkhala pakati wa Ummah صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati, 'Amene akusisita pa mutu wa mwana wamasiye chifukwa chongosangalatsa Allah عَزَّوَجَلَّ, adzalandira mphotho pa tsitsi lililonse lomwe anasisita. Ndipo amene akuchitira mwana wamasiye aliyense zabwino, ine ndi iye tidzakhala limodzi Kumwamba motero (ndiye kuti, zala ziwirizi zikukumana).' *(Musnad Imam Ahmad, vol. 8, pp. 272, Hadees. 22215)*

kusisita pa mutu wa mwana wamasiye ndi kupatsa chakudya Miskeen kumachotsa kuwuma kwa ntima. Sayyiduna Abu Hurayrah رَضِیَ اللّٰہُ عَنۡہُ anati kuti munthu wina anadandawula za kuwuma kwa ntima wake. Mtumiki Woyera صَلَّی اللّٰہُ عَلَیۡہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم anati, 'sisitani pa mutu wa mwana wamasiye ndipo dyetsani Osowa (Miskeen).'

*(Musnad Imam Ahmad, vol. 3, pp. 335, Hadees 9028)*

Mtumiki Wankulu komanso Woyera صَلَّی اللّٰہُ عَلَیۡہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم anati: 'Ngati mnyamata ali mwana wamasiye, sisitani mutu wake, pobweretsa dzanja kutsogolo; ndipo ngati abambo a mwanayo ali ndi moyo, sisitani mutu wake pobweretsa dzanja lake kukhosi kwake'.

*(Al-Mu'jam-ul-Awsat, vol. 1, pp. 351, Hadees 9028)*

صَلُّوۡا عَلَی الۡحَبِیۡب صَلَّی اللّٰہُ عَلٰی مُحَمَّد

## Yesetsani kusunga ubale ndi nkazi

Mwamuna ayenera kuchitira nkazi wake ubwino ndipo azithana naye mwanzeru. Mtumiki Wathu Wokondedwa صَلَّی اللّٰہُ عَلَیۡہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم anati, 'Nkazi anapangidwa kuchokera ku nthiti ndipo simungamuwongole. Ngati mukufuna kupeza phindu kuchokera kwa iye, mutha kuchita motero ndi kupindika kwake. Ngati mutayesa kumuwongola, mudzamuthyola ndipo kuthyola nkazi kumatanthawuza kumusudzula.' *(Sahih Muslim, pp. 775, Hadees 1468)*



www.dawateislami.net

## Ubwino wa kufatsa pa nkazi

Zimadziwika kuti nthawi zonse azikhala ndi zizolowezi zokhumudwitsa. Chimene mwamuna ayenera kuchita ndikukhala woleza ntima komanso wololera nthawi zonse. Mtumiki Woyera صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati, 'Mwa okhulupirira owona ndi amene ali ndi makhalidwe abwino komanso amene ali odekha kwambiri kwa nkazi wake.'

*(Sunan-ut-Tirmizi, vol. 4, pp. 278, Hadees 2621)*

## Khululakirani nkazi

Wokondedwa abale achisilamu! Amene amakalipira ngakhalenso kumenya akazi awo pa nkhani zazing'ono ayenera kuganizira Hadees iyi yodalitsika. Kugwiritsa ntchito mphanvu zachiwawa komanso zowopseza kwa amene ali ofowoka mwachibadwa sikukhala umamuna. Ngati nkazi akulakwitsa Moyiwala, mamuna ayenera kumukhululukira. Popeza amalandira ubwino wambiri kuchokera kwa iye, ayeneranso kulekerera zolakwa zake. Mtumiki wa Chifundo صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati, 'Mamuna wachisilamu sangakhale ndi chidani kwa nkazi wachisilamu. Ngati sakonda zizolowezi zake zilizonse, angapeze chizolowezi china chosangalatsa.'

*(Sahih Muslim, pp. 775, Hadees 1469)*

## Mchere wambiri mu chakudya

Zinanenedwa kuti nkazi wa munthu wina nthawi ina anasakaniza mchere wambiri mu chakudya. Iye anakwiya kwambiri koma anatha kukhala chete, kuganiza, 'Inenso ndimalakwitsa zambiri. Ngati ndingamuchitire nkhanza lero chifukwa cha kulakwitsa kwake, Allah عَزَّوَجَلَّ akhoza kundilanga chifukwa cha machimo anga pa Tsiku la Chiweruzo.' Motero, anakhululukira kulakwitsa kwa nkazi wake muntima. Atamwalira, munthu wina anamuwona mmaloto ake namufunsa, 'Kodi Allah anakuchitira chani?, iye anayankha, 'Mazunzo amayenera kuyikidwa pa ine malingana ndikuchuluka kwa machimo, pamene Allah anati, 'Kapolo wanga wankazi anayika mchere wochuluka muchakudya ndipo unamukhululukira, inenso ndikukukhululukira lero chifukwa cha chabwino chimene unachita.'

Chifukwa cha Mtumiki wokondedwa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم komanso chifukwa cha kuyenda ndi ma Madani Qafilah mwezi uliwonse, kulemba nkabuku konse ka Madani In'amaat ndikukapereka kwa m'bale woyenera kumayambiriro kwa mwezi uliwonse wa chisilamu, اِنْ شَآءَاللّٰه عَزَّوَجَلَّ, mudzapeza chikondi chachikulu cholemekeza Asilamu kotero kuti mikangano yanu yonse ndi achibale anu idzathetsedwa ndipo nawonso adzalowa mu chikhalidwe cha Madani cha Dawat-e-Islami, اِنْ شَآءَاللّٰه عَزَّوَجَلَّ.

*Soya huwa naseeb jaga di-jiye Huzoor*

*Meetha Madinah mujh ko dikha di-jiye Huzoor*

***kumasulira:*** *O Mtumiki wokondedwa* صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم*!*
*Ndipangeni ine kuwona Madina wokoma! Mulore kumweturira kwa mwayi kuwoneke pa ine*

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Ufulu wa mamuna

Nkazi nayenso ayenera kukhala wachifundo ndi wachikondi kwa mamuna wake. Mtumiki wopatulika صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati, 'ndikulumbira kwa Yemwe mphanvu zonse za moyo wanga zili m'manja mwake! kutakhala kuti mabala ali paliponse pathupi la mamuna kuyambira kumutu mpaka kumapadzi, omwe akutuluka mafinya amagazi, ndipo nkazi akuwanyambita, chomwecho akhala kuti sanakwaniritse ufulu wamamuna.'

*(Musnad Imam Ahmad, vol. 4, pp. 318, Hadees 12614)*

## Musachoke pakhomo lamamuna

Mayi amene amakonda kukangana ndi mamuna wake pa zinthu zing'ono-zing'ono ndiponso amene nthawi zambiri amapita kunyumba kwa makolo ake chifukwa cha mikangano, ayenera kuwerenga ma Hadith abwino awa mobwerezabwereza komanso ndikuwayika pantima. Mtumiki Woyera صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati: "Nkazi asatuluke m'nyumba ya mamuna wake popanda chilolezo chake. Ngati atuluka popanda chifukwa chofunika,

Mulungu عَزَّوَجَلَّ ndi angelo ake amamutemberera mpaka atapempha chikhulululukiro kapena kubwerera kunyumba ya mamuna wake". *(Kanz-ul-'Ummal, vol. 16, pp. 144, Hadees 44801)*

## Chifukwa chimene akazi ambiri akakhalire ku Gehena

Akazi ena amakhala osanvera kwambiri komanso osayamika kwa amuna awo. Ngakhale atakwiyitsidwa pang'ono chabe amayiwala zabwino zonse zimene mamuna wawo anawachitira ndipo amayamba kuwanyoza ndikuwachitira chipongwe. Akazi amene amakonda kulira, kudandawula komanso kulalatira amuna awo, ayenera kuphunzira phunziro kuchokera mu hadith iyi;

Mtumiki Wolemekezeka komanso Wodziwika kwambiri صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anali kupita ku Eid-Gah (malo opempherera Eid) pa tsiku la Eid. Iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anakumana ndi akazi ena m'njira ndipo anati: O inu akazi! Perekani chithandizo (chopereka), chifukwa ndawona ambiri a inu muli ku Gehena." Akaziwo anafunsa kuti: "Ya Rasoolallah صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم! Ndi chifukwa chani?" Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anayankha kuti: "Azimayi mumakonda kulalata ndikusayamika amuna anu."

*(Sahih Bukhari, vol. 1, pp. 123, Hadees 304)*

## Ufulu wa anthu oyandikana nawo



www.dawateislami.net

Wokondedwa abale anga achisilamu! aliyense ayenera kuchitira anzake oyandikana nawo ubwino ndi ulemu, pokhapokha ngati pali chifukwa chovomerezeka cha Shar'iah. Munthu wina anapita pa maso pa Mtumiki wokondedwa Muhammad صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم Ndipo anafunsa kuti: "Ya Rasulallah صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم! Kodi ndingadziwe bwanji ngati zomwe ndachita ndi zolondola kapena zolakwika?" Mtumiki wa Chifundo صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anayankha kuti: "Ukanva oyandikana nawo akunena kuti zomwe wachita ndi zabwino, ndiye kuti zomwe wachita ndi zabwino. Koma ukanva akunena kuti zomwe wachita ndi zolakwika, ndiye kuti walakwitsadi."

*(Ibn Majah, vol. 4, pp. 479, Hadees 4223)*

## Chiphaso cha makhalidwe abwino

اَللّٰهُ اَكْبَر! Tiyeni tiwone mmene oyandikana nawo alili ofunikira kwambiri! Ndi ngati satifiketi ya khalidwe labwino imaperekedwa ndi iwo. Tsoka ilo, masiku ano anthu ambiri samasamala za oyandikana nawo. Chifukwa cha chikondi cha Mtumiki wokondedwa Muhammad صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم, komanso chifukwa cha madalitso ochokera ku ulendo wa Madani Qafilah mwezi uliwonse, kulemba kabuku konse ka Madani In'amaat ndi kukapereka kwa m'bale wa Chisilamu amene ali ndi udindo mwezi uliwonse wa Chisilamu, اِنْ شَآءَاللّٰه عَزَّوَجَلَّ Mtima wathu udzayamba kuwona kufunika kwa oyandikana nawo.

Tidzakhala ndi maganizo abwino owalemekeza, ndipo dera lathu lidzakhala ngati munda wa Madinah, اِنْ شَآءَاللّٰہعَزَّوَجَلَّ

*Bahaar aaye mahallay mayn mayray bhi Ya Rasoolallah*

*Idhar bhi to jhari barsay koi rahmat kay baadal say*

*Masika afike m'mudzi mwanga, Ya Rasoolallah! Apa palinso nvula ikhale kuchokera mu ntambo wa chifundo!*

صَلُّوْا عَلَی الْحَبِیْب صَلَّی اللّٰہُ عَلٰی مُحَمَّد

## Kodi Mtsogoleri wa Qafilah akuyenera kukhala ndi makhalidwe otani?

Mtsogoleri pa ulendo ayenera kulemekeza ndi kutumikira anzake kwambiri.

Mtumiki Woyera صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati: "Munthu amene amatumikira anzake kwambiri pa ulendo ndiye Mtsogoleri, ndipo anzake sangamuposepo pa ntchito iliyonse yabwino. Komabe, ngati m'modzi wa iwo afera m'njira ya Mulungu (kukhala shaheed), ndiye ndipamene adzamupose."

*(Shu'ab-ul-Iman, vol. 6, pp. 334, Hadees 8407)*

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Chilichonse chokhala chowonjezera chiyenera kuperekedwa kwa ena

Nthawi ina, pa ulendo, Mtumiki Wokondedwa komanso Wodalitsika wa Allah صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati, "Aliyense amene ali ndi chida chowonjezera choyendera, apereke kwa amene alibe choyendera; ndipo aliyense amene ali ndi chakudya chowonjezera, apereke kwa amene alibe chakudya." Ndipo motero, iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anayankhula za zinthu zina zambiri. Sayyiduna Abu Sa'eed Khudri رَضِىَ اللّٰهُ عَنْهُ anati, "M'njira yomweyi, iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anatchula mitundu yosiyanasiyana ya katundu mpaka tinawona kuti palibe munthu amene ali ndi ufulu wosunga chilichonse chomwe ndi chowonjezera."

*(Sahih Muslim, p. 952, Hadees 1728)*

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Mudzafunsidwa za amene ali pansi panu

Sikuti Mtsogoleri-wa-Qafilah yekha, koma aliyense ayeneranso kuchitira zabwino anthu amene ali pansi pake. Mtumuiki Wankulu komanso Wopatulika kwambiri, (صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم), anati: "Aliyense wa inu ndi woyang'anira, ndipo aliyense

adzafunsidwa za udindo wake. Mfumu ndi woyang'anira ndipo adzafunsidwa za anthu ake. Ndipo mamuna ndi woyang'anira banja lake ndipo adzafunsidwa za amene ali pansi pake. Ndipo nkazi ndi woyang'anira wa nyumba ya mamuna wake ndipo adzafunsidwa za amene ali pansi pake."

*(Sahih Bukhari, vol. 2, pp. 112, Hadees 2409)*

Wokondedwa abale anga achisilamu! Chifukwa cha chikondi cha Mtumiki wokondedwa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم komanso madalitso obwera chifukwa choyenda nthawi zonse ndi ma Madani Qafilah mwezi uliwonse, kulemba kabuku konse ka Madani In'aamaat komanso kulipereka kwa m'bale wa Chisilamu amene ali ndi udindo mwezi uliwonse wa Chisilamu, اِنْ شَآءَاللّٰه عَزَّوَجَلَّ. mudzakhala ndi chidwi cholemekeza omwe ali pansi pa inu ndipo aliyense adzasangalala nanu ndi kukupempherani ndi mapemphero a ku Madina, اِنْ شَآءَاللّٰه عَزَّوَجَلَّ.

*Mayn dunya ki dawlat ka mangta nahin hoon*

*Mujhay bhaiyon! Do Du'a-e-Madinah*

Ine sindine wopemphapempha chuma cha padziko. Abale anga! Zomwe ndikufuna ndi pemphero la ku Madina.

صَلُّوْا عَلَی الْحَبِیْب     صَلَّی اللهُ عَلٰی مُحَمَّد

## Kugawa Ntchito

Panthawi ya ulendo, ntchito zosiyanasiyana ziyenera kugawidwa kwa oyenda m'malo moti katundu yense akhale pa munthu m'modzi yekha. Masahaba odalitsika رَضِیَ اللّٰہُ عَنۡہُم anali pa ulendo. Anaganiza zozinga mbuzi ndipo anagawana ntchito. Wina anatenga udindo wozinga mbuziyo, pomwe wina anatenga udindo wochotsa khungu. Wina anatenga ntchito yophika. Mneneri Wolemekezeka صَلَّی اللّٰہُ عَلَیۡہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم anati, 'Ndi udindo wanga kusonkhetsa nkhuni.' Masahaba ake odalitsika رَضِیَ اللّٰہُ عَنۡہُم anati, 'Ya Rasoolallah! Ifenso tigwira (ntchito imeneyo).' Mneneri Woyera صَلَّی اللّٰہُ عَلَیۡہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم anati, 'ndikudziwa kuti mugwira ntchito imeneyo mokondwera koma sindikufuna kukhala wotchuka pakati panu. Allah عَزَّوَجَلَّ safuna zimenezi.'

*(Khulasah Siyar Sayyid-ul-Bashar li-Muhibb-id-Deen At-Tabari, pp. 75, mwachidule)*

صَلُّوۡا عَلَی الۡحَبِیۡب صَلَّی اللّٰہُ عَلٰی مُحَمَّد

## Perekani mpando wanu kwa ena

Ngati mipando yonse ya galimoto kapena sitima yadzaza, apa ulendo okhala sayenera kukhala pansi ulendo wonse, komanso amene akuyima sayenera kuyima nthawi yonse. Aliyense ayenera kusinthana kukhala pansi kuti aliyense apeze mwayi wokhalako ndipo apeze mphotho popereka mpando wake kwa ena, malinga ndi momwe zinthu zilili. Munthu angapeze



www.dawateislami.net

mphotho ngakhale popereka mpando wake womwe anasungira, chifukwa sizoletsedwa kupereka mpando wake kwa ena.

Sayyiduna 'Abdullah Bin Mas'ood رَضِیَ اللّٰہُ عَنۡہُ ananena kuti panali ngamila imodzi yokha kwa anthu atatu pa nkhondo ya Badr. Choncho Sayyiduna Abu Lubabah ndi Sayyiduna 'Ali رَضِیَ اللهُ عَنۡهُمَا anagawana kukwera limodzi ndi Mtumiki Wopatsa Chifundo صَلَّى اللهُ عَلَيۡهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم. Onse awiriwo ananena kuti: Pamene kunali nthawi ya Mtumiki صَلَّى اللهُ عَلَيۡهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم kuyenda, ife tonse tinamupempha kuti akhale wokhala, ndipo ife tiyenda m'malo mwake. Mtumiki Wopatsa Chifundo صَلَّى اللهُ عَلَيۡهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anayankha kuti, 'Simuli amphanvu kundiposa, ndipo inenso (sikuti) sindisamala za mphotho.' (kutanthawuza kuti: Inenso ndifuna mphotho, n'chifukwa chani ndisayende?)

*(Sharh-us-Sunnah, vol. 5, pp. 566, Hadees 2680)*

## Ulendo ndi Madani Qafilah

Wokondedwa abale a Chisilamu! Pachifukwa cha Mtumiki wokondedwa صَلَّى اللهُ عَلَيۡهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ndipo ndi madalitso a kuyenda nthawi zonse ndi Madani Qafilah mwezi uliwonse, ndi kulemba nkabuku konse ka Madani In'amaat ndi kukapereka kwa m'bale wa Chisilamu amene ali ndi udindo mwezi uliwonse wa Chisilamu, اِنۡ شَآءَاللّٰہ عَزَّوَجَلَّ munthu adzakhala ndi chikhumbokhumbo chofuna kudzipereka mwa kupereka mpando wake kwa ena. Ndi madalitso ake, munthu adzadalitsidwa ndi ulendo wa Hajj komanso kuwona Madinah.

Kuphatikizapo, panthawi ya ma ulendo odalitsikawa, munthu adzapitiriza kukhala ndi mwayi wopereka mipando kwa apa ulendo ku Mina, Muzdalifah, ‘Arafat, Makkah ndi Madinah.

*Ya Rab! Su-ay Madinah mastanah ban kay jaoon*

*Us Sham’-e-Do Jahan ka parwanah ban kay jaoon*

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Usatenge malo ochuluka

Munthu sayenera kutenga malo ochuluka chifukwa cha ntendere wake pokhumudwitsa ena m'malo amene anthu amasonkhana ambiri monga, pa Ijtima’ah ndi zina zotero. Zanenedwa ndi Sayyiduna Sahl Bin Mu’aaz رَضِیَ اللهُ عَنْهُمَا, ‘Abambo anga olemekezeka رَضِیَ اللّٰهُ عَنْهُ anati, ‘Tinapita pa ulendo wa Jihad ndi Mtumiki Wopatulika صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم. Anthu anatenga malo ochuluka (pa ulendo), mpaka anatsekereza njira. Mtumiki Wopatulika صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anatumiza munthu kuti alengeze, ‘Ndithu, amene amatsekereza njira, palibe Jihad kwa iye’.

*(Sunan Abi Dawood, vol. 3, pp. 58, Hadees 2629)*

## Ndikutsatira Sunnah kupereka malo kwa amene akubwera kumene

Ndi Sunnah kwa anthu omwe akhala kale kuti apereke malo kwa amene akubwera kumene mwa kusuntha pang’ono. Zalembedwa

ndi Sayyiduna Waasilah Bin Khattab رَضِیَ اللّٰہُ عَنۡہُ kuti munthu wina anabwera kwa Mtumiki Wapamwamba صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم. Iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anakhala mu Mzikiti. Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anasuntha (ndiko kuti anasuntha kuti ampatse malo). Munthuyo anati, 'Ya Rasoolallah صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم! Malo anali kale okwanira. (N'chifukwa chani mwazivutitsa popanga malo ena?)' Mtumiki wa Chifundo صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anayankha kuti, 'Ufulu wa Msilamu ndi wakuti, akawona mchimwene wake, ayenera kumupatsa malo.' *(Shu'ab-ul-Iman, vol. 6, tsamba 468, Hadees 8933)*

Wokondedwa abale anga a Chisilamu! Pachifukwa cha Mtumiki Wokondedwa komanso Wodalitsika صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ndi chifukwa cha madalitso ochokera ku kuyenda mosalekeza ndi ma Madani Qafilah mwezi uliwonse, kulemba nkabuku konse ka Madani In'amaat komanso kukapereka kwa m'bale wa Chisilamu woyenerera mwezi uliwonse wa Chisilamu, اِنۡ شَآءَاللّٰہ عَزَّوَجَلَّ padzakhala madalitso ngakhale pamalo ochepa. Munthu adzalandira chilimbikitso chotsatira Sunnah yopatsa ena malo mwa kusuntha, ndipo adzadalitsidwa ndi malo aakulu mu Jannat-ul-Baqi', اِنۡ شَآءَاللّٰہ عَزَّوَجَلَّ.

*Zahideen-e-dunya bhi rashk kertay 'aasi per*

*Mayn Baqi'-e-gharqad mayn dafn ho agar jata*

*"Ngakhale anthu odzichepetsa a padziko lapansi akanandichitira nsanje — ine wochimwa, ngati ndikanayikidwa m'manda a Jannat-ul-Baqi'."*

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب     صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Kutsitsa mawu

Sayyiduna 'Abdullah Bin Mas'ood رَضِیَ اللّٰهُ عَنْهُ ananena kuti Mtsogoleri Wokondedwa wa Mulungu, M'busa Wathu Wopatulika صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati, 'Ngati pali anthu atatu, awiri mwa iwo sayenera kulankhula Mwachinsisi mopatula mmodzi yekha, mpaka anthu ambiri atafika pankumano chifukwa zimawawitsa mmodzi yekhayo.' *(Sahih Bukhari, vol. 4, pp. 185, Hadees 6290)*

(Mmodzi angaganize kuti akulankhula za iye kapena kuti sanamuyese kuti woyenera kukhala nawo pamtsonkhano.)

## Kudumpha m'makosi

Ngati anthu akhala kale mizere yakutsogolo pa Salat-ul-Jumu'ah, ndizoletsedwa kwa munthu kuti adumphe mmakosi mwa anthu kupita patsogolo. M'tsogoleri wa Chifundo, Nkhala pakati wa Ummah, صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati, 'Munthu amene adumpha pa mapewa a anthu pa tsiku la chisanu, wapanga Mlatho olowera ku Gahena.'

*(Sunan-ut-Tirmizi, vol. 2, pp. 48, Hadees 513)*

Imodzi mwa tanthawuzo lake ndi kuti anthu Adzakalowa ku Gahena pomudutsa (momupondaponda) iye. *(Bahar-e-Shari'at, vol. 1, pp. 761, 762)*

Wokondedwa abale anga Achisilamu! Munthu ayenera kufika ku Masjid pa Salat-ul-Jumu'ah nthawi yabwino. Ngati Wachedwa ndipo ulaliki wayamba, ayenera kukhala pomwe wafikira kupeza malopo ndipo asayende kupita kutsogolo. A'la Hadrat, Imam-e-Ahl-e-Sunnat, Maulana Shah Imam Ahmad Raza Khan رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anafotokoza kuti: Ndi Haram kuyenda pamene ulaliki ukuchitika. Katswiri Wophunzira za Chisilamu رَحِمَهُمُ اللّٰهُ anati, 'Ngati munthu afika ku Masjid pomwe ulaliki wayamba, ayenera kupeza malo pomwe wafikira. Asamayende kupita kutsogolo chifukwa ndi chinthu choletsedwa kupanga zinthu (kuyendayenda) ulaliki uli nkati.' *(Fatawa Razawiyyah – referenced, vol. 8, pp. 333)*

Iye رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anapitiriza kuti, 'kuyang'anayang'ana mbali zina ndi Haram pa nthawi ya ulaliki.' *(Ibid, p. 333)*

## Kulowelera anthu awiri popanda chilolezo

Ngati anthu awiri akhala kale, ndi chinthu chosafunikira kwambiri komanso chopanda ulemu kwa Msilamu kulowa pakati pawo popanda chilolezo chawo. Mtumiki wathu Wopatulika صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati, 'Sikuvomerezeka kwa munthu

kuwapangitsa anthu awiri kusiyana osapempha chilolezo chawo.' (Kutanthawuza kuti, sikuvomerezeka kukhala pakati pawo popanda chilolezo.)

Sayyiduna Huzayfah رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہُ ananena kuti Mtumiki Wathu Wopatulika صَلَّی اللّٰہُ عَلَیْہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم anati munthu amene amakhala (mosayitanidwa) pakati pa gulu ndiwotembeleredwa.

Mtumiki Wathu Wopatulika صَلَّی اللّٰہُ عَلَیْہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم anati, 'Munthu sayenera kupempha amene wakhala kuti achoke ndicholinga chakuti iye akhale pamalo pake. Koma amene akukhala ayenera kupanga malo (a mumthu wabwerayo).'

*(Sahih Muslim, pp. 1199, Hadees 2177)*

Mtumiki Wathu Wopatulika صَلَّی اللّٰہُ عَلَیْہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم anati, 'Ngati wachoka pa nkumano ndipo wabweranso, ndi woyenera kukhala pamalo amene anakhala.' *(Ibid, Hadees 2179)*

## Kusunga malo poyika nsalu

A'la Hadrat, Imam-e-Ahl-e-Sunnat, Maulana Shah Imam Ahmad Raza Khan رَحْمَةُ اللّٰہِ عَلَیْہ ananena: Ngati munthu afika ku Masjid, wakhala pamalo ndiyeno wapita kukachita Wudu, kwinaku atasiya nsalu ngati chizindikiro pa malo amene anakhalapo, munthu wina sayenera kukhala pamenepo Pochotsa nsaluyo chifukwa woyamba wakhalapo kale. Komabe, Kusunga kwa malo uku ndi kwa nthawi yochepa.

Mwachitsanzo, zimatenga mphindi zochepa chabe kupita kukachita Wudu, kusiya nsalu ndikubweranso. [Choncho ichi ndi chifukwa chovomerezeka]. Koma izi sizilola aliyense kuyika chinthu mu Masjid, kwanthawi zonse kuti awonekere kuti ndi wamphanvu kuposa ena pomwe afika ku Masjid. Izi sizikulola kapena kuvomerezeka konse.

*(Fatawa Razawiyyah, vol. 16, pp. 148)*

Wokondedwa abale anga achisilamu! Pachifukwa cha Mtumiki Wathu Wopatulika صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ndi m'phanvu ya ulendo wotsagana ndi Madani Qafilah mwezi uliwonse, kulemba nkabuku konse ka Madani In'amaat ndikupereka kwa m'bale wa chisilamu mwezi uliwonse wa Chisilamu, اِنْ شَآءَاللّٰه عَزَّوَجَلَّ, mudzaphunzira malamulo a kupita pamisonkhano, kukulitsa maganizo a kulemekeza Asilamu, kupewa kuwononga ufulu wa anthu ndi kuwakhudza ntima. Ndi madalitso a maphunziro a Madani, mudzalandira ufulu wochita Hajj, ndikukhala ku Madinah komanso ndi kuchita ma Sunnahwa kumeneko.

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب　　صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

## Musapweteke ntima wa munthu aliyense

Wokondedwa abale anga achisilamu! Ulemu kwa msilamu umafuna kuti tikwaniritse ufulu wa Msilamu aliyense pantengo uliwonse. Sitiyenera kuwononga ntima wa Msilamu aliyense

popanda chilolezo cha Shari'a. Mtumiki Wathu Wopatulika صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم sanapwetekepo ntima wa Msilamu aliyense. Iye sanakayikirepo aliyense, Sananyozepo aliyense, sanamuwopsezepo aliyense, komanso sanachitepo chipongwe aliyense. M'malo mwake, iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم amamuthandiza aliyense (kutanthawuza kuwonetsa chikondi kwa aliyense).

## Uswa-e-Hasanah

Kuti tidziwe mmene tingalemekezere Asilamu moyenera, tiyenera kutsatira ndi kuyika maganizo athu pa 'Uswa-e-Hasanah' (makhalidwe abwino kwambiri) a Mtumiki wathu Wokondedwa ndi Wodalitsika صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم. Allah عَزَّوَجَلَّ akunena mu Qur'an Yawulemerero, gawo 21, Surah Al-Ahzaab, vesi 21:

لَقَدْ كَانَ لَكُمْ فِيْ رَسُوْلِ اللّٰهِ اُسْوَةٌ حَسَنَةٌ

*Ndithudi kutsatira Mneneri Wolemekezeka wa Allah nkwabwino kwa inu.*

*[Kanz-ul-Iman (Kumasulira kwa Qur'an)] (Gawo 21, Al-Ahzaab, vesi 21)*

## Ena mwa makhalidwe abwino a Mtumiki Woyera ﷺ

Mneneri wa anthu, Mtendere wa mu ntima ndi maganizo athu, Wopatsa kwambiri komanso Wokoma ntima صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ndithudi ndi wolemekezeka kwambiri, wawulemu kwambiri komanso wotchuka kwambiri. Ndi udindo wathu wa ukulu

kumulemekeza iye nthawi zonse. Tsopano, ndikufuna kutchula ena mwa makhalidwe ake abwino omwe adzatitsogolere pa nkhani yolemekeza Msilamu.

1. Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم nthawi zonse ankateteza lilime lake lodalitsika ndipo amangolankhula zofunikira zokha zokha.

2. Iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم amakhala ndi anthu mwachikondi. Iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم sanachite chilichonse chomwe chingayambitse chidani.

3. Iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم nthawi zonse ankalemekeza 'munthu wolemekezeka' wa dziko ndipo ankamusankha kukhala mtsogoleri wa dzikolo.

4. Iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم nthawi zonse amalangiza anthu kuwopa Allah عَزَّوَجَلَّ.

5. Iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم nthawi zonse amafunsa za abwenzi odalitsika رَضِیَ اللهُ عَنْهُم.

6. Iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم nthawi zonse amatamanda zokambirana ndi malingaliro abwino a anthu ndipo amadzudzula chilichonse choyipa ndipo amaletsa anthu kuchita zimenezo.

7. Iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ankachita chilichonse mofatsa.

8. Iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم sanali wosanyalanyaza kusintha kwa anthu.

9. Iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم nthawi zonse ankakumbukira Allah عَزَّوَجَلَّ.

10. Akapita kwinakwake, iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ankafikira kulikonse kumene wapeza malo ndipo ankalangiza ena kuchita chimodzimodzi.

11. Iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم amakwaniritsa ufulu wa anthu omwe amakhala naye.

12. Aliyense amene anali ndi mwayi wokhala pa ubwenzi wodala wa Mtumiki Woyera صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ankanva kuti Mtumiki Woyera صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم amamukonda kwambiri.

13. Iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم sankamaliza kukambirana ndi aliyense mpaka munthuyo atachoka yekha.

14. Akagwirana chanza ndi wina, iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم sankachotsa manja ake odalitsika poyamba.

15. Iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم nthawi zonse amathandiza osowa.

16. Iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم amachitira aliyense Mowolowa manja komanso mwa ulemu.

17. Misonkhano yake yodala inali misonkhano ya chidziwitso, kulekerera, kudzichepetsa, kuleza ntima ndi chikhulupiriro.

18. Misonkhano yake yodala inali yantendere kwambiri ndipo palibe amene ananyozedwa.

19. Ngati wina analakwitsa pamisonkhano yodala, sizinafalikire. *(Shumaail-ut-Tirmizi, tsamba 192-193, mwachidule)*

20. Iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ankayika maganizo ake onse polankhula ndi wina. *(Shu'ab-ul-Iman, Hadees 1430)*

21. Iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم sankayang'ana nkhope ya aliyense. *(Ihya-ul-'Uloom, vol. 2, tsamba 442)*

22. Iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anali wamanyazi kwambiri kuposa mbeta. *(Shumaail-ut-Tirmizi, tsamba 203)*

23. Iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم nthawi zonse amayamba ndi Salam. *(Shu'ab-ul-Iman, Hadees 1430)*

24. Iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ankaperekaso Salam kwa ana.

25. Iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ankanena Labbayk [Ndili pano] aliyense akamuyitana. *(Wasail-ul-Wusool, tsamba 207)*

26. Iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم sanali kutambasula miyendo yake yodala kwa anthu pamisonkhano.

27. Iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم nthawi zambiri amakhala atayang'ana ku Qiblah.

28. Iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم sanabwereze kwa aliyense pa chifukwa chilichonse.

29. M'malo mobwezera, iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم nthawi zonse amakhululukira omwe amamuvutitsa. *(Ihya-ul-'Uloom, vol. 2, tsamba 448, 449)*

30. Kupatula Jihad, iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم Sanakanthepo aliyense ndi manja ake odalitsika. Ngakhale akazi ake ndi akapolo. *(Shumaail-ut-Tirmizi, tsamba 197)*

31. Iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ankalankhula mofatsa. *(Ihya-ul-'Uloom, vol. 2, tsamba 451)* Hadith yodala imanena kuti, 'Pa Tsiku Lomaliza, munthu woyipa kwambiri pakati pa anthu pamaso pa Allah عَزَّوَجَلَّ ndi yemwe anthu anamusiya chifukwa cha mawu ake oyipa.' *(Sahih Muslim, tsamba 1398, Hadith 2591)*

32. Iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ankalankhula mofatsa kwambiri moti aliyense anatha kuwerenga mawu omwe iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ankanena. *(Sahih Bukhari, Hadith 3567)*

33. Iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anali wofatsa mwachibadwa ndipo amakhalabe wosangalala.

34. Iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم sanali kufuwula konse.

35. Iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم sanalankhule mwawukali konse.

36. Iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم sanali kudzudzula anthu konse.

37. Iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم sanali wamithulo konse.

38. Iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anadzitchinjiriza ku zinthu zitatu: kukangana, kudzikuza ndi kudziphatika ku ntchito zosafunika.

39. Iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم sanali kupeza zolakwika za anthu.

40. Iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anangonena zomwe zinali chifukwa cha mphoto [kwa iye].

41. Iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم amakhala woleza ntima ngakhale ndi mafunso akuluakulu a mlendo.

42. Iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم sanali kusokoneza kukambirana kwa aliyense. Ngati wina anapita patali, iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ankamletsa kapena kuchoka pamalo pake. *(Shumaail-ut-Tirmizi, tsamba 199-200, mwachidule)*

43. Kunali kukhazikika kwake kwakukulu kuti iye صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم sanali kukhazikika pa malo enieni okhala. *(Akhlaq-un-Nabi, tsamba 15)*

44. Iye صَلَّى اللهُ عَلَيۡهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم nthawi zina Amapumira pa mphasa ndipo nthawi zina pansi popanda kuyalapo chilichonse. *(Wasail-ul-Wusool, tsamba 189)*

45. Iye صَلَّى اللهُ عَلَيۡهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم sanali kuseka [mokweza moti ena ngati analipo akananva]. *(Ihya-ul-'Uloom, vol. 2, tsamba 446)*

46. Abwenzi odalitsika رَضِیَ اللهُ عَنۡهُم anafotokoza kuti Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللهُ عَلَيۡهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم amamwetulira kwambiri (pamisonkhano yoyenera).

*(Ihya-ul-'Uloom, vol. 2, tsamba 453)*

Sayyiduna 'Abdullah Bin Haaris رَضِیَ اللهُ عَنۡهُ anafotokoza kuti sanawone aliyense akumwetulira kwambiri kuposa Mtumiki Woyera صَلَّى اللهُ عَلَيۡهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم.

*(Shumaail-ut-Tirmizi, tsamba 136)*

صَلُّوۡا عَلَى الۡحَبِيۡب صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

Ayi abale achisilamu! Pomaliza nkhani yanga, ndikupempha mwayi wotchula ma Sunnah ena, madalitso a Sunnah ndi makhalidwe ena abwino. Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللهُ عَلَيۡهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati, 'Amene akonda Sunnah yanga, amandikonda ine ndipo amene amandikonda ine, adzakhala nane Kuparadizo.'

*(Ibn 'Asakir, vol. 9, tsamba 343)*

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

◆◆◆

## Kudula ubale ndiko Haram: Ngale 13 za Madani

Allah عَزَّوَجَلَّ ananena mu Qur'an Yoyera:

وَاتَّقُوا اللّٰهَ الَّذِیۡ تَسَآءَلُوۡنَ بِهٖ وَ الۡاَرۡحَامَ ؕ

*Ndipo opani Allah, Amene ndi Dzina Lake mumapemphana (ufulu wanu kuchokera kwa wina ndi mzake) ndipo samalirani maubale anu a magazi.*

*[Kanz-ul-Iman (Kumasulira kwa Qur'an)] (Gawo 4, An-Nisa, vesi 1)*

Ponena za vesi lomwe ladutsa, likunenedwa mu Tafseer Mazhari: Kutanthawuza, pewani kudula ma ubale.

*(Tafseer Mazhari, vol. 2, tsamba 3)*

## Mawu Asanu ndi Awiri a Mtumiki Woyera صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَسَلَّم

1. Wokhulupirira mwa Allah عَزَّوَجَلَّ ndi Tsiku Lachimaliziro ayenera kuchitira achibale mwachikondi. *(Sahih Bukhari, vol. 4, tsamba 136, Hadith 6138)*

2. Pa Tsiku Lachimaliziro, anthu amitundu itatu adzakhala pansi pa nthunzi wa 'Arsh wa Allah عَزَّوَجَلَّ. Mmodzi amene amachitira achibale mwachikondi (adzakhala mwa iwo). *(Al-Firdaus bima Saur-ul-Khattab, vol. 2, tsamba 99, Hadith 2526)*

3. Amene adule ma ubale sadzalowa Kuparadizo. *(Sahih Bukhari, vol. 4, tsamba 97, Hadith 5984)*

4. Wabwino pakati pa anthu onse ndi amene amawerenga Qur'an Yoyera kwambiri, amakhala woyera kwambiri, amayitanira [anthu] ku chabwino ndipo amawaletsa [iwo] ku zoyipa kwambiri ndipo amachitira achibale ake mwachikondi kwambiri.' *(Musnad Imam Ahmad, vol. 10, tsamba 402, Hadith 27504)*

5. Mosakayikira, Sadaqah yabwino kwambiri ndi yomwe yaperekedwa kwa wa chibale yemwe ali ndi chidani chobisika. *(Ibid, vol. 9, tsamba 138, Hadith 23589)*

6. Ngati pali munthu wodula ubale pakati pa gulu, chifundo cha Allah عَزَّوَجَلَّ sichitsika pamenepo. *(Az-Zawajir, vol. 2, tsamba 153)*

7. Amene akufuna kuti nyumba ya ufumu imangidwe kwa iye Kumwamba ndipo ma nyota ake akwezedwe, ayenera kukhululukira yemwe amamukanikiza, kupatsa yemwe

amamunyenga, ndikukhazikitsa ubale ndi yemwe amadula ubale naye. *(Al Mustadrak, vol. 3, tsamba 12, Hadith 3215)*

- Sayyiduna Faqih Abul Lays Samarqandi رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه ananena: Pali zikhalidwe khumi zakuchitira achibale mwachikondi: Zimabweretsa chisangalalo cha Allah عَزَّوَجَلَّ. Zimakondweretsa anthu. Zimakondweretsa angelo. Zimakupatsani matamando kuchokera kwa Asilamu. Zimakwiyitsa Satana. Zimawonjezera zaka. Zimabweretsa madalitso mu chakudya. Zimakondweretsa makolo akufa (kutanthawuza kuti abambo ndi agogo achisilamu). Zimayambitsa mgwirizano. Zimawonjezera mphoto pambuyo pa infa chifukwa anthu amapempherera munthu wotere. *(Tanbih-ul-Ghafileen, tsamba 73)*

- Zikunenedwa patsamba 558 mpaka 560 la buku la 3 la buku la Bahar-e-Shari'at lamasamba 1196 lofalitsidwa ndi Maktaba-tul-Madinah, nthambi yosindikiza ya Dawat-e-Islami: ﴿صِلَةُ رِحْم﴾ [Silah-Rihm] kutanthawuza kukhazikitsa ma ubale, kutanthawuza kuchitira achibale chilichonse chabwino ndi kuwachitira mwachikondi. Ummah wonse wagwirizana kuti Silah-Rihm ndi Wajib ndipo kudula ma ubale ndiko Haram. Kodi achibale otani amene ayenera kuchitiridwa mwachikondi ngati wa Wajib? Akatswiri ena ananena kuti ndi 'Zu-Rihm Mahram' ndipo ena ananena kuti ndi achibale a Zu-Rihm

mosasamala kanthu ngati ndi Mahram kapena ayi. Mwachidziwikire, lamulo lachiwiri ndilo lolondola kwambiri. Ahadees ali ndi lamulo losasunthika la kuchitira achibale mwachikondi. Qur'an Yoyera inanenanso mosasunthika ﴿ذَوِی الْقُرْبٰی﴾ (kutanthawuza kuti achibale).

Komabe, popeza pali milingo yosiyana ya ma ubale, palinso milingo yosiyana ya kuchitira achibale mwachikondi. Makolo ali ndi udindo wa ukulu kwambiri. Pambuyo pa iwo pali udindo wa 'Zu-Rihm Mahram' (kutanthawuza achibale amene kuchita nawo ukwati ndi Haram kwamuyaya chifukwa cha ubale wa Nasabi [kutanthawuza wabanja]). Pambuyo pa iwo pali udindo wa achibale otsala, kutengera ubale wapafupi womwe ali nawo. *(Rad-dul-Muhtar, vol. 9, tsamba 678)*

- ❖ Munthu akhoza kuchitira achibale ake mwachikondi m'njira zosiyanasiyana. Mwachitsanzo, kuwapatsa mphatso, kuwathandiza ngati akufunika thandizo, kuwatonthoza ndi Salam, kukumana nawo, kulankhula nawo ndi kuwachitira mwa ulemu komanso ubwino. *(Durad, vol. 1, tsamba 323)*

- ❖ Ngati munthu ali kudziko lachilendo, ayenera kukhala akulankhulana ndi achibale ake kuti ubale usaduke. Ngati n'kotheka, ayenera kubwera kudziko lake kuti ubale ndi achibale ake ulimbe. Izi zidzakulitsanso mgwirizano pakati

pa achibale. *(Rad-dul-Muhtar, vol. 9, tsamba 678)* (Kuwayimbira achibale kapena kukhala akulumikizana nawo pa intaneti ndikofunikanso kwambiri.)

- Kuchita bwino sikungotanthawuza kuchitira bwino achibale okha amene anakuchitiranі bwino. Izi ndizochitikadi 'kusinthana kwachikondi'. Mwachitsanzo, kutumiza mphatso kwa chibale yemwe wakutumizirani mphatso kapena kupita kunyumba kwa yemwe amabwera kwanu. Kwenikweni, kuchitira bwino kumatanthawuza kukhazikitsa ubale ndi yemwe amakudulani, ndipo kusamalira chibale amene akukunyalanyazani ndi kukuchokerani. *(Ibid)*

Kuti muphunzire ma Sunnah masawuzande ambiri, gulani ndikuwerenga mabuku awiri ofalitsidwa ndi Maktaba-tul-Madinah: (1) Bahar-e-Shari'at gawo 16 lamasamba 312 (2) Sunnatayn aur Adaab lamasamba 120. Njira ina yabwino yophunzirira ma Sunnah ndiyo kuyenda ndi Madani Qafilah a Dawat-e-Islami ndi wonkonda Rasool.

*Lootnay rahmatayn Qafilay mayn chalo*

*Seekhnay Sunnatayn Qafilay mayn chalo*

*Haun gi hal mushkilayn Qafilay mayn chalo*

*Khatm haun shamatayn Qafilay mayn chalo*

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب          صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

**Muhammad Ilyas Attar Qadiri**

10 Safar-ul-Muzaffar, 1436 AH (December 3, 2014)



www.dawateislami.net


الحمد لله رب العلمين والصلوة والسلام على سيد المرسلين اما بعد فاعوذ بالله من الشيطن الرجيم ؕ بسم الله الرحمن الرحيم ؕ

## Mphotho ya kuyang'ana Msilamu ndi chikondi

Mawu a Hadith:

Mtumiki Wokondedwa (صلی اللہ علیہ وآلہ وسلم) anati: Msilamu amene agwirana chanza ndi m'bale wake pamene alibe chidani m'mitima mwawo kwa wina ndi mnzake, Allah (عزوجل) adzawakhululukira machimo awo am'mbuyo manja awo asanalekane, ndipo aliyense amene angoyang'ane m'bale wake Msilamu ndi chikondi ndipo alibe chidani naye mumtima mwake, ndiye kuti machimo am'mbuyo a onse awiri adzakhululukidwa asanayang'ane kwina.

*(Kanz-ul-'Ummal, vol. 9, juzuu 57, Hadees 25358)*



ISBN 978-969-631-697-8
0109370

Aalami Madani Markaz, Faizan-e-Madinah, Mahallah Saudagaran
Purani Sabzi Mandi, Bab-ul-Madinah, Karachi, Pakistan.
UAN: +92 21 111 25 26 92 | Ext: 1262
Web: www.dawateislami.net | E-mail: translation@dawateislami.net